# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Davide

1. Samueli adzoza Davide akhale mfumu
2. Davide apha Goliati
3. Davide ayenera kuzemba
4. Davide aleka Sauli osamupha
5. Davide alowa ufumu
6. Chimo loopsa la Davide
7. Davide acitira Mefiboseti cifundo

Ndi mtumiki wanga Davide adzakhala mfumu yao, ndipo iwo onse adzakhala ndi mbusa mmodzi, adzayendanso m'maweruzo anga, nadzasunga malemba anga ndi kuwacita – Ezekieli 37.24

- Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Samueli adzoza Davide akhale mfumu

**1 Samueli 16.1-13**

1. Ndipo Yehova ananena ndi Samueli, Iwe ukuti ulire cifukwa ca Sauli nthawi yotani, popeza Ine ndinamkana kuti asakhale mfumu ya Israyeli? Dzaza nyanga yako ndi mafuta, numuke, ndidzakutumiza kwa Jese wa ku Betelehemu; pakuti ndinadzionera mfumu pakati pa ana ace.
2. Ndipo Samueli anati, Ndikamuka bwanji? Sauli akacimva, adzandipha. Ndipo Yehova anati, Umuke nayo ng'ombe yaikazi, nunene kuti, Ndadza kudzaphera nsembe kwa Yehova.
3. Ndipo uitane Jese abwere kunsembeko, ndipo Ine ndidzakusonyeza cimene uyenera kucita; ndipo udzandidzozera iye amene ndidzakuchulira dzina lace.
4. Ndipo Samueli anacita cimene Yehova ananena, nadza ku Betelehemu. Ndipo akuru a mudziwo anadza kukomana naye monthunthumira, nati, Mubwera ndi mtendere kodi?
5. Nati iye, Ndi mtendere umene; ndadza kudzaphera nsembe kwa Yehova; mudzipatule ndi kufika ndi ine kunsembeko. Ndipo iye anapatula Jese ndi ana ace, nawaitanira kunsembeko.
6. Ndipo kunali, pakufika iwo, iye anayang'ana pa Eliyabu, nati, Zoonadi, wodzozedwa wa Yehova ali pamaso pace.
7. Koma Yehova ananena ndi Samueli, Usayang'ane nkhope yace, kapena kutalika kwa msinkhu wace, popeza Ine ndinamkana iye; pakuti Yehova saona monga aona munthu; pakuti munthu ayang'ana cooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mumtima.
8. Pamenepo Jese anaitana Abinadabu nampititsa pa Samueli. Ndipo iye adati, Koma uyunso Yehova sadamsankha.
9. Pamenepo Jese anapititsapo Sama. Ndipo anati, Koma uyunso Yehova sanamsankha.
10. Ndipo Jese anapititsapo ana ace amuna asanu ndi awiri. Koma Samueli anati kwa Jese, Yehova sanawasankha awa.
11. Ndipo Samueli anati kwa Jese, Ana anu ndi omwewa kodi? Nati iye, Watsala wina, mng'ono wa onse, ndipo taonani, iye alikuweta nkhosa. Ndipo Samueli anati kwa Jese, Tumiza munthu akamtenge; pakuti ife sitidzakhala pansi kufikira iye atadza kuno.
12. Ndipo anatumiza munthu, nabwera naye. Tsono iye anali wofiirira, ndi wa nkhope yokongola, ndi maonekedwe okoma. Ndipo Yehova anati, Nyamuka umdzoze, pakuti ndi ameneyu.
13. Pamenepo Samueli anatenga nyanga ya mafuta, namdzoza pakati pa abale ace; ndipo mzimu wa Yehova unalimbika pa Davide kuyambira tsiku lomweli. Ndipo Samueli ananyamuka, nanka ku Rama.

**Mafunso**

1. Kodi Mulungu anaitana yani kukadzoza mfumu yatsopano? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi tate Jese anali ndi ana angati? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Davide anali kuti pamene wina wake anadza kumuitana?  Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Samueli anadzoza motani mfumu yatsopano? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Chulani dzina la mfumu yatsopano. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Mulungu anapatsa Davide nchito yaikulu ndiyo kulamulira dziko lonse. Kodi mumapempherera anthu olamulira kuti alamulire bwino?

**Sewero**

Ikani mau awa m’ndandanda. Mwacitsanzo: m u g u n l u -> mulungu

1. m u m f u
   Yankho: m……………………………………………
2. d i d v a e
   Yankho: d…………………………………………….
3. m a f a t u
   Yankho: m……………………………………………
4. g n a y a n
   Yankho: n…………………………………………….
5. w a z d o z e d o w
   Yankho: w…………………………………………….
6. t a m i m
   Yankho: m…………………………………………….

## 2. Davide apha Goliati

**1 Samueli 17.1-11**

1. Pamenepo Afilisti anasonkhanitsa makamu ao a nkhondo, naunjikana ku Soko wa ku Yuda, namanga zithando pakati pa Soko ndi Azeka ku Efesi-damimu.
2. Ndipo Sauli ndi anthu a Israyeli anasonkhana, namanga zithando pa cigwa ca Ela, nandandalitsa nkhondo yao kuti akaponyane ndi Afilisti.
3. Ndipo Afilisti anaima paphiri tsidya lija, ndi Aisrayeli anaima paphiri tsidya lina; ndi pakati pao panali cigwa.
4. Ndipo ku zithando za Afilisti kunaturuka ciwinda, dzina lace Goliate wa ku Gati, kutalika kwace ndiko mikono isanu ndi umodzi ndi cikhato.
5. Ndipo anali ndi cisoti camkuwa pamutu pace, nabvala maraya aunyolo, olemera ngati masekeli zikwi zisanu za mkuwa,
6. nakuta msongolo wace ndi cobvala camkuwa, ndiponso pacikota pace panali nthungo yamkuwa.
7. Ndipo mtengo wa mkondo wace unali ngati mtanda woombera nsaru; ndi khali la mkondowo linalemera ngati masekeli mazana asanu ndi limodzi a citsulo; ndipo womnyamulira cikopa anamtsogolera.
8. Naima iye naitana makamu a nkhondo a Israyeli, nanena nao, Munaturukiranji kundandalitsa nkhondo yanu? Sindine Mfilisti kodi, ndi inu anyamata a Sauli? mudzisankhire munthu, atsikire kwa ine.
9. Akakhoza iyeyo kuponyana ndi ine ndi kundipha, tidzakhala ife akapolo anu; koma ine ndikamlaka, ndi kumupha, tsono mudzakhala inu akapolo athu, ndi kutitumikira ife.
10. Nati Mfilistiyo, Ine ndinyoza makamu a nkhondo a Israyeli lero; mundipatse munthu, kuti tilimbane ife awiri.
11. Ndipo pamene Sauli ndi Aisrayeli onse anamva mau ao a Mfilistiyo, anadodoma, naopa kwambiri.

**1 Samueli 17.31-51**

31. Ndipo pamene mau adanena Davide anamveka, anawapitiriza kwa Sauli; ndipo iye anamuitana.
32. Ndipo Davide anati kwa Sauli, Asade nkhawa munthu ali yense cifukwa ca iyeyo; ine kapolo wanu ndidzapita kuponyana ndi Mfilisti uyu.
33. Ndipo Sauli anati kwa Davide, Sukhoza iwe kukomana ndi Mfilisti uyu kukaponyana naye; pakuti iwe ndiwe mnyamata, koma iye anazolowera nkhondo kuyambira ubwana wace.
34. Ndipo Davide anati kwa Sauli, Ine kapolo wanu ndinalikusunga nkhosa za atate wanga; ndipo pakubwera mkango, mwina cimbalangondo ndi kutenga nkhosa ya gululo,
35. ndinacithamangira, ndi kucikantha, ndi kuiturutsa m'kamwa mwace; ndipo pamene cinaneliukira, ndinagwira cowa lace ndi kucikantha ndi kucipha.
36. Ine kapolo wanu ndinapha mkango ndi cimbalangondo zonse ziwiri; ndipo Mfilisti uyu wosadulidwa adzakhala ngati mmodzi wa izo, popeza wanyoza makamu a Mulungu wamoyo.
37. Nati Davide, Yehova wakundipulumutsa pa mphamvu ya mkango, ndi mphamvu ya cimbalangondo, Iyeyu adzandipulumutsa m'dzanja la Mfilisti uyu, Ndipo Sauli anati kwa Davide, Muka, Yehova akhale nawe.
38. Ndipo Sauli anabveka Davide zobvala zace za iye yekha, nambveka cisoti camkuwa pamutu pace, nambvekanso maraya aunyolo.
39. Ndipo Davide anamanga lupanga lace pamwamba pa zobvala zace, nayesa kuyenda nazo; popeza sanaziyesera kale. Ndipo Davide anati kwa Sauli, Sindikhoza kuyenda ndi izi; pakuti sindinazizolowera. Nazibvula Davide.
40. Natenga ndodo yace m'dzanja lace nadzisankhira miyala isanu yosalala ya mumtsinje, naiika m'thumba la kubusa, limene anali nalo ndilo cibete; ndi coponyera miyala cinali m'dzanja lace, momwemo anayandikira kwa Mfilistiyo.
41. Ndipo Mfilistiyo anadza, nayandikira kwa Davide; ndi wonyamula cikopa cace anamtsogolera.
42. Ndipo Mfilisti pakumwazamwaza maso, ndi kuona Davide, anampeputsa; popeza anali mnyamata cabe, wofiirira, ndi wa nkhope yokongola.
43. Ndipo Mfilisti anati kwa Davide, Ine ndine garu kodi, kuti iwe ukudza kwa ine ndi ndodo? Ndi Mfilistiyo anatukwana Davide nachula milungu yace.
44. Ndipo Mfilistiyo anati kwa Davide, Idza kuno kwa ine, ndidzapatsa mnofu wako kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za kuthengo.
45. Ndipo Davide anati kwa Mfilistiyo, Iwe ukudza kwa ine ndi lupanga, ndi mkondo, ndi nthungo; koma ine ndafika kwa iwe m'dzina la Yehova wa makamu, Mulungu wa ankhondo a Israyeli amene iwe unawanyoza.
46. Lero lino Yehova adzakupereka iwe m'dzanja langa, ndipo ndidzakukantha, ndi kukucotsera mutu wako. Ndipo lero ndidzapatsa mitembo ya makamu a Afilisti kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za dziko lapansi; kuti dziko lonse likazindikire kuti kwa Israyeli kuli Mulungu.
47. Ndi msonkhano wonse uno udzazindikira kuti Yehova sapulumutsa ndi lupanga, kapena ndi mkondo; pakuti Yehova ndiye mwini nkhondo, ndipo iye adzakuperekani inu m'manja athu.

48. Ndipo kunali, pamene Mfilistiyo anadzikonza, nadza, nasendera pafupi kuti akomane ndi Davide, Davide anafulumira, nathamangira ku khamulo, kuti akomane ndi Mfilistiyo.
49. Ndipo Davide anapisa dzanja lace m'thumba mwace, naturutsamo mwala, nauponya, nalasa Mfilistiyo pamphumi; ndi mwalawo unalowa m'mphumi, ndipo iye anagwa pansi cafufumimba.
50. Comweco Davide anapambana Mfilistiyo ndi mwala wa coponyera cace, nakantha Mfilistiyo, namupha. Koma m'dzanja la Davide munalibe lupanga.
51. Potero Davide anathamanga naima pa Mfilistiyo, nagwira lupanga lace, nalisolola m'cimace, namtsiriza nadula nalo mutu wace. Ndipo pakuona Afilisti kuti ciwinda cao cidafa, anathawa.

**Mafunso**

1. Ncifukwa ciani Davide anafuna kupha Goliati? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Nanga ife tiyenera kucita ciani pamene munthu anyoza Mulungu?
3. Ncifukwa ciani mfumu Sauli sanafune Davide kukomana ndi Goliati? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
4. Kodi Davide anadziwa bwanji kuti adzakwaniritsa kupha Goliati? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Kodi Davide anapambana bwanji Goliati? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
6. Kodi tingaphunziremo ciani m'nthano iyi?
7. Kodi kukhala ndi bwenzi wosamvera ndi kwabwino?

## 3. Davide ayenera kuzemba

**1 Samueli 16.14-23**

14. Koma mzimu wa Yehova unamcokera Sauli, ndi mzimu woipa wocokera kwa Yehova unambvuta iye.
15. Ndipo anyamata a Sauli ananena naye, Onani tsopano, mzimu woipa wocokera kwa Mulungu ulikubvuta inu.
16. Tsono inu mbuye wathu muuze anyamata anu, amene ali pamaso panu, kuti afune munthu wanthetemya wodziwa kuyimba zeze; ndipo kudzakhala, pamene mzimu woipa wocokera kwa Mulungu uli pa inu, iyeyo adzayimba ndi dzanja lace, ndipo mudzakhala wolama.
17. Ndipo Sauli anati kwa anyamata ace, Mundifunire tsono munthu wakudziwa kuyimba bwino, nimubwere naye kwa ine.
18. Ndipo mnyamata wace wina anayankha, nati, Taonani, ine ndaona mwana wa Jese wa ku Betelehemu, ndiye wanthetemya wodziwa kuyimbira, ndipo ali wa mtima wolimba ndi woyenera nkhondo, ndiponso ali wocenjera manenedwe ace; ndiye munthu wokongola, ndipo Yehova ali naye.
19. Cifukwa cace Sauli anatumiza mithenga kwa Jese, nati, Unditumizire Davide, mwana wako, amene ali kunkhosa.
20. Ndipo Jese anatenga buru namsenza mkate, ndi thumba la vinyo, ndi: mwana wa mbuzi, nazitumiza kwa Sauli ndi Davide mwana wace.
21. Ndipo Davide anafika kwa Sauli, naima pamaso pace; ndipo iye anamkonda kwambiri, namsandutsa wonyamula zida zace.
22. Ndipo Sauli anatumiza kwa Jese, nati, Ulole kuti Davide aime pamaso panga; pakuti ndamkomera mtima.
23. Ndipo kunali kuti pamene mzimu woipawo wocokera kwa Mulungu unali pa Sauli, Davide anatenga zeze, naliza ndi dzanja lace; comweco Sauli anatsitsimuka, nakhala bwino, ndi mzimu woipa unamcokera iye.

**1 Samueli 19.1-10**

1. Ndipo Sauli analankhula kwa Jonatani mwana wace, ndi anyamata ace onse kuti amuphe Davide.
2. Koma Jonatani mwana wa Sauli anakondwera kwambiri ndi Davide. Ndipo Jonatani anauza Davide, nati, Sauli atate wanga alikufuna kukupha; cifukwa cace tsono ucenjere m'mawa, mukhale m'malo mosadziwika, nubisale;
3. ndipo ine ndidzaturuka ndi kuima pa mbali ya atate wanga kumunda kumene kuli iwe, ndipo ndidzalankhula ndi atate wanga za iwe; ndipo ndikaona kanthu ndidzakudziwitsa.
4. Ndipo Jonatani analankhula ndi atate wace mobvomereza Davide, nanena naye, Mfumu asacimwire mnyamata wace Davide; cifukwa iyeyo sanacimwira inu, ndipo nchito zace anakucitiranі zinali zabwino ndithu;
5. popeza iye anataya moyo wace nakantha Mfilistiyo, ndipo Yehova anacitira Aisrayeli onse cipulumutso cacikuru, inu munaciona, nimunakondwera; tsono mudzacimwiranji mwazi wosalakwa, ndi kumupha Davide popanda cifukwa?
6. Ndipo Sauli anamvera mau a Jonatani; nalumbira, Pali Yehova, sadzaphedwa iye.
7. Pamenepo Jonatani anaitana Davide, namuuza zonsezi. Ndipo Jonatani anafika naye Davide kwa Sauli, iye nakhalanso pamaso pace monga kale.
8. Ndipo kunalinso nkhondo; ndipo Davide anaturuka, nakamenyana ndi Afilisti, nawapha ndi maphedwe akuru, ndipo iwo anamthawa iye.
9. Ndipo mzimu woipa wocokera kwa Yehova unali pa Sauli, pakukhala iye m'nyumba mwace, ndi mkondo wace m'dzanja lace; ndipo Davide anayimba ndi dzanja lace.
10. Ndipo Sauli anayesa kupyoza Davide kumphatikiza kukhoma ndi mkondowo; koma iye anadzilanditsa kucoka pamaso pa Sauli; ndipo analasa khoma; ndipo Davide anathawa napulumuka usiku uja.

**Mafunso**

1. Ndi ciani cimene cinali kubvuta Sauli? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Kodi azimai anaimba nyimbo iti pamene Davide anabwera kucokera atapha Afilistiwo? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene cinacitika kwa Sauli atamva nyimboyo? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
4. Kodi nciani ciani comwe Sauli anaponya kwa Davide? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Kodi ndani amene anapulumutsa Davide?

**Sewero.** Pezani mau onse.

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| R | D | G | B | P | O | S | M |
| S | A | U | L | I | L | W | Z |
| A | V | Z | M | A | I | U | I |
| H | I | A | T | A | T | E | M |
| P | D | J | P | T | B | M | U |
| U | E | O | D | N | O | K | M |
| K | G | Y | E | H | O | V | A |

mzimu
Sauli
Davide
Yehova
kupha
mkondo
atate

**4. Davide aleka Sauli osamupha**

**1 Samueli 24**

1. Ndipo kunali, pakubwerera Sauli potsata Afilisti, anamuuza, kuti, Taonani, Davide ali ku cipululu ca Engedi.
2. Tsono Sauli anatenga anthu zikwi zitatu osankhika pakati pa Aisrayeli onse, namuka kukafuna Davide ndi anthu ace m'matanthwe a zinkhoma.
3. Ndipo panjira anafika ku makola a nkhosa, kumene kunali phanga; ndipo Sauli analowa kuti akapfunde mapazi ace. Ndipo Davide ndi anyamata ace analikukhala m'kati mwa phangamo,
4. Ndipo anyamata a Davide ananena naye, Onani, lero ndilo tsiku limene Yehova anati kwa inu, Onani, Ine ndidzapereka mdani wako m'dzanja lako, kuti ukamcitira iye cokukomera. Ndipo Davide ananyamuka, nadula mkawo wa mwinjiro wa Sauli mobisika.
5. Ndipo kunali m'tsogolo mwace kuti a mtima wa Davide unamtsutsa cifukwa adadula mkawo wa mwinjiro wa Sauli.
6. Nati kwa anyamata ace, Mulungu andiletse kucitira ici mbuye wanga, wodzozedwa wa Yehova, kumsamulira dzanja langa, popeza iye ndiye wodzozedwa wa Yehova.
7. Comweco Davide analetsa anyamata ace ndi mau awa, osawaloleza kuukira Sauli. Ndipo Sauli ananyamuka, naturuka m'phangamo, namuka njira yace.
8. Bwino lace Davide yemwe ananyamuka, naturuka m'phangamo, napfuulira Sauli, nati, Mbuye wanga, mfumu. Ndipo pakuceuka Sauli, Davide anaweramira nkhope yace pansi, namgwadira.
9. Davide nanena ndi Sauli, Bwanji mulikusamalira mau a anthu akuti, Onani, Davide afuna kukucitirani coipa.
10. Onani, lero lomwe maso anu anapenya kuti Yehova anakuperekani inu lero m'dzanja langa m'phangamo, ndipo ena anandiuza ndikupheni; koma ndinakulekani, ndi kuti, Sindidzatukulira mbuye wanga dzanja langa; cifukwa iye ndiye wodzozedwa wa Yehova.
11. Ndiponso atate wanga, penyani, inde penyani mkawo wa mwinjiro wanu m'dzanja langa; popeza ndinadula mkawo wa mwinjiro wanu, osakuphani, mudziwe, nimuone kuti mulibe coipa kapena kulakwa m'dzanja langa, ndipo sindinakucimwirani, cinkana inu musaka moyo wanga kuti muugwire,
12. Yehova aweruze pakati pa ine ndi inu; ndipo Yehova adzandibwezera cilango kwa inu; koma dzanja langa silidzakhala pa inu.
13. Monga umanena mwambi wa makolo, kuti, Ucimo uturukira mwa ocimwa; koma dzanja langa silidzakhala pa inu.
14. Nanga mfumu ya Israyeli inaturukira yani; inu mulikupitikitsa yani? Garu wakufa, kapena nsabwe.
15. Cifukwa cace Yehova akhale woweruza, naweruze pakati pa ine ndi inu, nayang'anire, oandigwirire moyo, oandipulumutse m'dzanja lanu.
16. Ndipo kunali, pakutsiriza Davide kulankhula mau awa kwa Sauli, Sauli anati, Ndiwo mau ako kodi, mwana wanga Davide? Sauli nakweza mau ace, nalira misozi.
17. Nati kwa Davide, Iwe ndiwe wolungama woposa ine; popeza unandibwezera zabwino, koma ine ndinakubwezera zoipa.
18. Ndipo unatsimikiza lero lino kuti wandicitira zabwino cifukwa sunandipha pamene Yehova anandipereka m'dzanja lako.
19. Pakuti munthu akapeza mdani wace, adzamleka kodi kuti acoke bwino? Cifukwa cace Yehova akubwezere zabwino pa ici unandicitira ine lero lomwe.
20. Ndipo tsono taona ndidziwa kuti udzakhala mfumu ndithu, ndi kuti ufumu wa Israyeli udzakhazikika m'dzanja lako.
21. Cifukwa cace tsono undilumbirire ndi Yehova, kuti sudzatha mbeu yanga nditamuka ine, ndi kuti sudzaononga dzina langa m'nyumba ya atate wanga.
22. Ndipo Davide analumbirira Sauli. Sauli namuka kwao; koma Davide ndi anthu ace anakwera kumka kungaka.

**Mafunso**

1. Kodi Sauli anatenga anthu angati kukasakhira Davide? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Sauli sanaphedwe atalowa m'phanga limodzimodzi lomwe Davide anali kubisalamo. Kodi Davide anacita ciani m'malo mwa kumupha Sauli? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Kodi Davide ananena ciani pamene anaitana Sauli kunja kwa phanga? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
4. Sauli anadabwa cifukwa Davide sanamuphe iye angakhale anali mdani wake. Ndi ciani comwe Sauli anacita pamene Davide anatha kulankhula? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Kodi Sauli anadziwa kuti Davide adzakhala mfumu? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

**5. Davide alowa ufumu**

**1 Samueli 31.1-8**

1. Ndipo Afilisti anaponyana ndi Aisrayeli; Aisrayeli nathawa pamaso pa Afilisti, nagwa olasidwa m'phiri la Giliboa.
2. Ndipo Afilisti anapitikitsa, osawaleka Sauli ndi ana ace; ndipo Afilisti anapha Jonatani, ndi Abinadabu, ndi Malikisua, ana a Sauli.
3. Ndipo nkhondoyo inamkulira Sauli kwambiri, oponya mibvi nampeza; ndipo iye anasautsika kwakukuru cifukwa ca oponya mibviyo.
4. Tsono Sauli ananena ndi wonyamula zida zace, Solola lupanga lako, undipyoze nalo; kuti osadulidwa awa angabwere ndi kundipyoza, ndi kundiseka, Koma woo nyamula zida zace anakana; cifukwa anaopa ndithu. Cifukwa cace Sauli anatenga lupanga lace naligwera.
5. Ndipo pakuona kuti Sauli anafa, wonyamula zida zace yemwe, anagwera lupanga lace, nafera limodzi ndi iye.
6. Comweco adamwalira pamodzi Sauli ndi ana ace atatu, ndi wonyamula zida zace, ndi anthu ace onse, tsiku lomwe lija.
7. Ndipo pamene Aisrayeli akukhala tsidya lina la cigwa, ndi iwo akukhala tsidya la Yordano, anaona kuti Aisrayeli alikuthawa, ndi kuti Sauli ndi ana ace anafa, iwowa anasiya midzi yao, nathawa; ndipo Afilisti anadza nakhala m'menemo.
8. Ndipo kunali m'mawa mwace, pakubwera Afilisti kubvula akufawo, anapeza Sauli ndi ana ace atatu ali akufa m'phiri la Giliboa.

**2 Samueli 1.1-12**

1. Ndipo kunali atamwalira Sauli, pamene Davide anabwera atawapha Aamaleki, ndipo Davide atakhala ku Zikilaga masiku awiri;
2. pa tsiku lacitatu, onani, munthu anaturuka ku zithando za Sauli, ali ndi zobvala zace zong'ambika, ndi dothi pamutu pace; ndipo kunatero kuti iye, pofika kwa Davide, anagwa pansi namgwadira.
3. Ndipo Davide ananena naye, Ufumira kuti iwe? iye nanena naye, Ndapulumuka ku zithando za Israyeti.
4. Ndipo Davide ananena naye, Kunaonekanji? undiuze. Nayankha iye, Anthu anathawa kunkhondo, ndipo ambiri anagwa nafa; ndipo Sauli ndi Jonatani mwana wace anafanso.
5. Ndipo Davide ananena ndi mnyamata wakumuuza, Udziwa bwanji kuti Sauli ndi Jonatani mwana wace anafa?
6. Mnyamata wakumuuzayo nati, Pamene ndinangoyenda pa phiri la Giliboa, ndinaona, Sauli alikuyedzamira nthungo yace, ndi magareta ndi apakavalo anamyandikiza.
7. Ndipo iye pakuceukira m'mbuyo mwace anandiona, nanditana. Ndipo ndinayankha, Ndine.
8. Nanena, Ndiwe yani? Ndipo ndinayankha kuti, Ndine M-amaleki.
9. Ndipo anati kwa ine, Uime pa ine nundiphe, cifukwa kuwawa mtima kwandigwera ine, popeza ndikali moyobe.
10. M'mwemo ndinakhala pambali pace ndi kumtsiriza cifukwa ndinadziwa kuti sangakhalenso ndi moyo wace, atagwa. Ndipo ndinatenga korona wa pamutu pace, ndi cigwinjiri ca pa mkono wace, ndabwera nazo kuno kwa mbuye wanga.
11. Pomwepo Davide anagwira zobvala zace nazing'amba; nateronso anthu onse okhala naye.
12. Nabuma, nalira misozi, nasala kudya kufikira madzulo, cifukwa ca Sauli ndi mwana wace Jonatani, ndi anthu a Yehova, ndi banja la Israyeli, cifukwa adagwa ndi lupanga.

**2 Samueli 2.1-7**

1. Ndipo zitatha izi Davide anafunsira kwa Yehova nati, Kodi ndikwere kunka m'mudzi wina wa Yuda? Ndipo Yehova ananena naye, Kwera. Davide nanena naye, Ndikwere kuti? Ndipo anati, Ku Hebroni.
2. Comweco Davide anakwera kunka kumeneko pamodzi ndi akazi ace awiri, ndiwo Ahingamu Mjezreeli, ndi Abigayeli mkazi wa Nabala wa ku Karimeli.
3. Ndipo Davide anakwera nao anyamata ace okhala naye, munthu yense ndi banja lace; iwowa nakhala m'midzi ya Hebroni.
4. Ndipo anthu Ayuda anabwera namdzoza Davide pomwepo akhale mfumu ya nyumba ya Yuda. Ndipo wina anauza Davide kuti, Anthu a ku Jabezi Gileadi ndiwo amene anamuika Sauli.
5. Pamenepo Davide anatumiza mithenga kwa anthu a ku Jabezi Gileadi, nanena nao, Mudalitsike ndi Yehova inu, popeza munacitira cokoma ici mbuye wanu Sauli, ndi kumuika.
6. Ndipo tsopano Yehova acitire inu cokoma ndi coonadi; inenso ndidzakubwezerani cokoma ici, popeza munacita cinthuci.
7. Cifukwa cace tsono manja anu alimbike, nimucite camuna; pakuti Sauli mbuye wanu wafa, ndi a nyumba ya Yuda anandidzoza ndikhale mfumu yao.

**Mafunso**

1. Mnyamata wobwera kwa Davide anacokera kuti? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Kodi mnyamatayo anadziwa bwanji kuti Sauli ndi Jonatani anamwalira? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene mnyamatayo anatenga cocokera kwa Sauli nampatsa Davide? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
4. Kodi Davide anasangalala pakumva za imfa ya Sauli ndi Jonatani? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Davide anasanduka mfumu. Analamulira dziko. M'mtima wake Mulungu analamulira. Kodi Mulungu alamulira inunso? Kodi Mulungu ndiye Mfumu m'njira yanji?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao.

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| G | | | | | | | |
| | | N | | | | | |
| | | | | | | G | |
| | | M | | | | | |
| | | | V | | | | |
| | | | | | | I | |

anafa
mfumu
Davide

Giliboa
Hebroni
anafa

**6. Chimo loopsa la Davide**

**2 Samueli 11.1-5, 26 ndi 27**

1. Ndipo kunali pofikanso caka, nyengo yakuturuka mafumu, Davide anatumiza Yoabu, pamodzi ndi anyamata ace, ndi Aisrayeli onse; ndipo iwo anasakaza ana a Amoni, naumangira misasa yankhondo Raba. Koma Davide anatsaliraku Yerusalemu.
2. Ndipo kunali pa madzulo Davide anauka pa kama wace nayenda pa tsindwi la nyumba ya mfumu. Ndipo iye ali patsindwipo anaona mkazi alinkusamba; ndi mkaziyo anali wocititsa kaso pomuyang'ana.
3. Ndipo Davide anatumiza munthu nafunsa za mkaziyo. Ndipo wina anati, Sindiye Bateseba, mwana wamkazi wa Eliyamu mkazi wa Uriya Mhiti?
4. Ndipo bavide anatumiza mithenga, namtenga iye; iye nabwera kwa iye, ndipo anagona naye, pakuti adacoka mumsambo; ndipo anabwereranso ku nyumba yace.
5. Ndipo mkaziyo anaima, natumiza munthu nauza Davide, kuti, Ndiri ndi pakati.
(…)
26. Ndipo pamene mkazi wa Uriya anamva kuti Uriya mwamuna wace adamwalira, iye analira maliro a mwamuna wace.
27. Ndipo pakuturuka malirowo, Davide anatumiza munthu namtenga afike kwao ku nyumba yace; ndipo iyeyo anakhala mkazi wace nambalira mwana wamwamuna. Koma Yehova anaipidwa ndi cinthu cimene Davide adacita.

**2 Samueli 12.1-9 ndi 13**

1. Ndipo Yehova anatumiza Natani kwa Davide. Ndipo anafika kwa iye nanena naye, Pa mudzi wina panali anthu awiri; wina wolemera, wina wosauka.
2. Wolemerayo anali nazo zoweta zazing'ono ndi zazikuru zambiri ndithu;
3. koma wosaukayo analibe kanthu kena koma kamwana kakakazi ka nkhosa, kamene anakagula ndi kukaweta; ndipo kameneko kanakula naye pamodzi ndi ana ace. Kanadyako cakudya cace ca iye yekha, kanamwera m'cikho ca iye yekha, kanagona pa cifukato cace, ndipo kanali kwa iye ngati mwana wace wamkazi.
4. Ndipo kwa wolemerayo kunafika mlendo, ndipo iye analeka kutengako mwa zoweta zace zazing'ono ndi zazikuru, kuphikira mlendo amene anafika kwa iye, koma anatenga mwana wa nkhosa wa wosaukayo, naphikira munthu amene anafika kwa iye.
5. Pamenepo mkwiyo wa Davide unayaka ndithu pa munthuyo, nati kwa Natani, Pali Yehova, munthu amene anacita ici, ayenera kumupha;
6. ndipo adzabwezera mwa mwana wa nkhosayo ena anai, cifukwa anacita ici osakhala naco cifundo.
7. Ndipo Natani ananena kwa Davide, Munthuyo ndi inu nomwe. Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Ndinakudzoza ukhale mfumu ya Israyeli, ndinakupulumutsa m'dzanja la Sauli;
8. ndinakupatsa nyumba ya mbuye wako, ndi akazi a mbuye wako pa cifukato cako, ndinakupatsanso nyumba ya Israyeli ndi ya Yuda; ndipo zimenezi zikadakucepera ndikadakuonjezera zina zakuti zakuti.
9. Cifukwa ninji unapeputsa mau a Yehova ndi kucita cimene ciri coipa pamaso pace? Unakantha Uriya Mhiti ndi lupanga ndi kutenga mkazi wace akhale mkazi wako; ndipo unamupha iye ndi lupanga la ana a Amoni.
(…)
13. Ndipo Davide anati kwa Natani, Ndinacimwira Yehova. Natani nati kwa Davide, Ndiponso Yehova wacotsa chimo lanu, simudzafa.

**Mafunso**

1. Kodi mfumu Davide anaona yani pamene anayenda pa tsindwi la nyumba ya mfumu? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Kodi mwamuna wake wa Bateseba anali yani? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Uriya anamwalira cifukwa ca ciwembu ca Davide. Kenaka Davide anakwatira Bateseba. Kodi Mulungu anamva bwanji pa zimene Davide adacita? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi ndani amene anatuma mneneri Natani kwa mfumu Davide? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Kodi munthu wosauka anali ndi nkhosa zingati? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
6. Kodi munthu wolemera anacita coipa cotani? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
7. Ndi cifukwa ciani Natani ananena kwa Davide: munthuyo ndi inu nomwe?
8. Kodi Davide anamva bwanji atamva mau a Natani? Ndi m’ndime iti momwe mwapeza yankho?
9. Davide analakalaka cinthu cimene sicinali cake. Kodi inunso mumakhumba zimene siziri zanu?

**7. Davide acitira Mefiboseti cifundo**

**2 Samueli 9**
1. Ndipo Davide anati, Kodi atsalako wina wa nyumba ya Sauli, kuti ndimcitire cifundo cifukwa ca Jonatani?
2. Ndipo panali mnyamata wa m'nyumba ya Sauli dzina lace Ziba; ndipo anamuitana iye afike kwa Davide; ndi mfumuyo inanena naye, Iwe ndiwe Ziba kodi? Nati iye, Ndine mnyamata wanu ame.
3. Ndipo mfumu inati, Kodi atsalanso wina wa nyumba ya Sauli kuti ndimuonetsere cifundo ca Mulungu? Ziba nanena ndi mfumu, Aliponso mwana wa Jonatani wopunduka mapazi ace.
4. Ndipo mfumu inanena naye, Ali kuti iyeyo? Ziba nanena kwa mfumu, Onani ali m'nyumba ya Makiri, mwana wa Amiyeli ku Lodebara.
5. Pamenepo Davide anatumiza anthu nakatenga iye ku nyumba ya Makiri mwana wa Amiyeli ku Lodebara.
6. Ndipo Mefiboseti mwana wa Jonatani, mwana wa Sauli, anafika kwa Davide, nagwa nkhope yace pansi, namlambira. Ndipo Davide anati, Mefiboseti! Nayankha iye, Ndine mnyamata wanu.
7. Ndipo Davide ananena naye, Usaopa, pakuti zoonadi ndidzakucitira kukoma mtima cifukwa ca Jonatani atate wako; ndi minda yonse ya Sauli ndidzakubwezera, ndipo udzadya pa gome langa cikhalire.
8. Ndipo iye anamlambira, nati, Mnyamata wanu ndani, kuti mulikupenya garu wakufa monga ine.
9. Pomwepo mfumu inaitana Ziba, mnyamata wa Sauli, ninena naye, Za Sauli zonse ndi za nyumba yace yonse ndampatsa mwana wa mbuye wako.
10. Ndipo uzimlimira munda wace, iwe ndi ana ako ndi anyamata ako; nuzibwera nazo zipatso zace kuti mwana wa mbuye wako akhale ndi zakudya; koma Mefiboseti, mwana wa mbuye wako, adzadya pa gome langa masiku onse. Ndipo Ziba anali nao ana amuna khumi ndi asanu, ndi anyamata makumi awiri.
11. Pomwepo Ziba anati kwa mfumu, Monga mwa zonse mfumu mbuye wanga mulamulira mnyamata wanu, momwemo adzacita mnyamata wanu. Tsono Mefiboseti, anadya pa gome la Davide monga wina wa ana a mfumu.
12. Ndipo Mefiboseti anali ndi mwana wamwamuna wamng'ono, dzina lace ndiye Mika. Ndipo onse akukhala m'nyumba ya Ziba anali anyamata a Mefiboseti.
13. Comweco Mefiboseti anakhala ku Yerusalemu, pakuti anadya masiku onse ku gome la mfumu, ndipo anali wopunduka mapazi ace onse awiri.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la mnyamata wa m'nyumba ya Sauli. Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Chulani dzina la mwana wa Jonatani. Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Ndi cifukwa ciani Mefiboseti anaopa kukomana ndi Davide?
4. Davide anacitira cifundo Mefiboseti. Cifukwa ciani anacita tero? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Mwa Ambuye tipeze cifundo. Kodi ici citanthauza ciani?
6. Kodi Davide analonjezera ciani Mefiboseti kulingana ndi m'ndime ya 7?
7. Davide anacita zimene analonjeza. Mulungu amacitanso zomwe analonjeza. Kodi mudziwako lonjezo la Mulungu la m'Baibulo? Chulani lonjezo imodzi.
8. Kodi tingaphunziremo ciani m'nthano iyi?

**Sewero**
Lembani malembo pa malo ao.

Salimo 86.3

| 13 | 21 | 14 | 4 | 9 | 3 | 9 | 20 | 9 | 18 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | |

| 3 | 9 | 6 | 21 | 14 | 4 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 1 | 13 | 2 | 21 | 25 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

# Mau a pa mtima

**Salimo 27.1b**

Yehova ndiye mphamvu ya moyo wanga; ndidzacita mantha ndi yani?

**Salimo 59.16**

Koma ine, ndidzayimbira mphamvu yanu; Inde ndidzayimbitsa cifundo canu mamawa: Pakuti Inu mwakhala msanje wanga, Ndi pothawirapo ine tsiku la nsautso yanga.

**1 Samueli 24.12**

Yehova aweruze pakati pa ine ndi inu; ndipo Yehova adzandibwezera cilango kwa inu; koma dzanja langa silidzakhala pa inu.

**Agalatiya 6.10**

Cifukwa cace, monga tiri nayo nyengo, ticitire onse cokoma, koma makamaka iwo a pa banja la cikhulupiriro.

**Salimo 23.1**

Salimo la Davide. Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa.

**1 Mbiri 11.9**

Ndipo Davide anakulakulabe, pakuti Yehova wa makamu anali naye.

## Sewero

Pezani mau onse.
Kenaka lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa.

Davide ananena:

.......................................................................................................................................................................

| | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| M | E | F | I | B | O | S | E | T | I | M |
| Z | I | G | O | M | E | A | Y | E | H | B |
| O | T | O | O | D | N | U | F | I | C | U |
| W | S | A | M | U | E | L | I | V | A | S |
| E | I | J | G | O | L | I | A | T | I | A |
| T | L | E | N | D | A | V | O | H | E | Y |
| A | I | S | R | A | Y | E | L | I | A | I |
| B | F | S | M | U | N | D | A | Y | M | E |
| E | A | E | N | Y | U | M | B | A | B | I |
| S | Z | E | Z | E | M | B | G | N | U | N |
| E | a | S | O | H | K | N | U | T | Y | A |
| T | A | N | A | S | A | A | W | H | E | T |
| A | U | R | I | Y | A | A | N | U | G | A |
| B | J | O | N | A | T | A | N | I | A | N |

| | | |
|---|---|---|
| mbusa<br>Bateseba<br>Jonatani<br>Yehova<br>Jese<br>Aisrayeli<br>cifundo<br>Uriya | Afilisti<br>munda<br>gome<br>nkhosa<br>nyumba<br>zoweta<br>ana<br>anthu | Mefiboseti<br>Sauli<br>Goliati<br>Samueli<br>Natani<br>nyanga<br>zeze<br>Ambuye |